


# Zomwe Mulongo wa Vusi Ananena


Nina Orange
Wiehan de Jager
Sitwe Benson Mkandawire
4
Chichewa ny



Tsiku limodzi m’mamawa, agogo a Vusi anamuitana, “Vusi, ndikupempha kuti upeleke Dzila ku makolo yako. Afuna kupanga keke yaikulu yapa cikwati ca mulongo wako.”



Munjila poyenda kumakolo, Vusi anakumana ndi anyamata awiri amene anali kuthyola ziphaso. Munyamata umodzi anatenga dzila lomwe linali ndi Vusi ndikuiphwanya pacimtengo. Dzila linaphwanyika.



“Kodi ndi cani cimene wacita?” Vusi analira. Dzila lija linali la keke. Iyo keke inali yapacikwati ca mlongo wanga. Kodi mlonga wanga azanena cani ngati palibe keke pacikwati?”



Anyamata anaphepetsa ponena Vusi. “Sitingathandizire pa nkhani ya keke, koma tenga kumtengo aka koyendela ukapase mlongo wako,” umodzi mwa iwo anatelo. Vusi anapitiliza ndi ulendo wake.



Munjila anakumananso ndi amuna awiri amene anali kumanga nyumba. Tingasewenzese ako kamtengo kokosa? Mwamuna umodzi anafunsa. Koma kamtengo sikanali kokosa ndiponso kanathyoka.



“Kodi ndi cani cimene mwacita?” Vusi analira. Ako kamtengo inali mphaso ya mlonga wanga. Anthu otenga zipaso anandipasa cifukwa anaphwanya dzila la keke. Keke inali ya cikwati ca mlongo wanga. Manje kulibe dzila, kulibe keke, ndiponso kulibe mphaso. Kodi mlonga wanga azanena cani?



Omanga nyumba anaphepetsa pothyola kumtengo. “Sitingathandizire pa nkhani ya keke, koma tenga cipagizo camauzi ukapase mlongo wako,” umodzi pa omanga anatelo. Vusi anapitiliza ndi ulendo wake.




Poyenda munjila, Vusi anakumana ndi mulimi na ng’ombe. “Cipangizo camauzu caoneka bwino, unganipaseko kang’ono? ng’ombe inafunsa. Cipangizo camauzu cinawama kwimbiri ndiponso, ngombe inadya conse.



“Kodi ndi cani cimene wacita?” Vusi analira. Ico cipangizo ca mauzu cinali mphaso ya mlonga wanga. Anthu omanga manyumba anandipasa cifukwa anathyola kamtengo kamene anandipasa othyola zipaso. Othyola zipaso anandipasa kamtengo cifukwa anaphanya dzila la keke la mlongo wanga. Keke inali ya cikwati ca mlongo wanga. Manje kulibe dzila, kulibe keke, ndiponso kulibe mphaso. Kodi mlonga wanga azanena cani?



Ng’ombe inaphepetsa pokudya kacipango. Mulimi anamupasa ng’ombe kukhala mphaso ya mlongo wa Vusi. Vusi anapiliza ulendo wake.



Koma ng'ombe inathawila kumwine wake pa cakudya ca m'madzulo. Vusi anasowa paulendo wake. Anafika mocedwa kwambiri pacikwati ca mlongo wake. Alendo anayamba kalekale zakudya pacikwati.



“Kodi ndizacita cani?” Vusi analira. Ngo’mbe yamene inathawa inali mphaso, m’malo mwa cipangizo ca mauzu cimene anandipasa omanga manyumba. Anthu omanga manyumba anandipasa cifukwa anathyola kamtengo kamene anandipasa othyola zipaso. Othyola zipaso anandipasa kamtengo cifukwa anaphanya dzila la keke la mlongo wanga. Keke inali ya cikwati ca mlongo wanga. Manje kulibe dzila, kulibe keke, ndiponso kulibe mphaso.



Mlongo wa Vusi anaganiza kwambili ndiponso anati, “Vusi mbale wanga, sindifuna za mphaso. Sindifunanso keke! Tilitonse pano pamodzi, diye camene candikondweletsa. Manje vala zovala zabwino mwakuti tisangalalale lelo. Izo ndiye zamene anacita Vusi.

# Global Storybooks

globalstorybooks.net

## Zomwe Mulongo wa Vusi Ananena


Nina Orange
Wiehan de Jager
Sitwe Benson Mkandawire


CC BY